




Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

TINGAKULE BWANJI



MWA

AMBUYE

8 LIPS (CYCLE)



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures


(KAFUKUFUKU WA MOYO WA ZOMERA)

TINGAKULE BWANJI MWA AMBUYE

(KAFUKUFUKU WA MOYO ZOMERA)

(A STUDY OF

Lolembedwa ndi
Jerry ndi Von Sommerville



Copyright, 1994, 1996 Frontlets
Publications, Rialto, CA.

Uthenga ochokera kwa olemba

Timakhulupilira kuti Yesu Khristu ndiye olenga zinthu zonse, zakale ndi zatsopano zomwe. Ndipo popanda iye panalibe chilichonse cholengedwa (Yohane 1:3). iziso titha kugwiritsa ntchito ku sayansi ya makono ano. Ngakhale kuti kuzindikila mkono wa Mulungu ndi kosowa mu nkhani ya maphunziroa ku sukulu.kupatulako maphunziro a za chipembedzo, koma pali mpata waukulu makamaka ku maphunziro a sayansi. Anthu tinatenga ulemelero

[WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021](#)

How to Grow in the Lord Lesson2 Outline



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

onse ku nkhani yopititsa patsogolo miyoyo ya anthu. Timayesetsa ndi mtima wathu onse kuchotsa mphanvu ya Umulungu wake kuchita pa ife. Munthu ndiye amene amagotengeka chab.

Monga maphunziro a kunyumba a chikhristu, khumbo lathu ndi kuonetsa ana anthu kupezeka kwa Mulungu ndi mphanvu yake komanso dzanja lake mu kuumba ndi kukonza dzikoli mu magawo awa (kale, tsopano ndi m'tsogolo) kuchokera kwa oyamba ndi otsiriza (alefa ndi omega). Maphunziro a sayansi ya chikhalidwe cha zinthu, zinthu zomwe Mulungu anakonza. Mulungu sitingamulekanitse ndi sayansi chifukwa iye ndi komwe sayansi inachokera.

KHRISTU OLENGA – MUNTHU NDIYE OTSANZIRA

Jerry ndi Von sommerville

CHIYAMBI

Mulungu adagwiritsa ntchito zitsanzo zambiri zooneka ndi Maso mu mau ake a m'Baibulo kuti afotokozere choonadi cha uzimu izi zili chomwechi kaamba kakuti ife anthu timavetsetsa mnanga zithu zooneka ndi maso. Mafanizo ndio khani zazifupi zomwe zimafotokozera choonadi cha dziko lathu lalooneka ndi masoli. Koma ku maso onunikilidwa ndi mau a Mulungu, nkhani izi zimaphuzitsa mfundo za uzimu za kukula mu chukhristu.

Mufanizo la ofesa mulibe kupatulapo, mu phunziro la kuthupi ndi ka phunziro kakafupi komwe kakuonetsera makulidwe a mbeu. Imodzi mwa mbeu zinayi zija ndi yomwe inakula ndi kuchuluka komaso kubala zipatso. Ku Ezekieli, Masalimo ndi mabuku ena a m'baibulo Mulungu anafanizira Munthu ndi mtima wake ngati zomera (mtengo) omwe ulinso panso ndondomeko zomwezo zoonenka mu zomera, zomera zathu za mu uzimu zingathekukula ndi kubala chipatso chochuluka.

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021


How to Grow in the Lord Lesson2 Outline



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

Tingakule bwanji mwa Ambuye ndi kafukufuku otsatana wa zinthu za uzimu ndi za thupi zomwe moyang'ana umoyo wa zomera. Phunziro lililonse likhoza kumalizidwa mu sabata imodzi kapena masabata ochulukirapo kuti ziphunzitsidwe mwa tsatanetsatane. Makolo kutsimikiza madera a kuthupi ndi ku uzimu komwe za madera ofunikira kwa ana, maganizo oonjezera kafukufuku wa sayansi yemwe atha kuphatikizidwa sabata iliyonse mogwirizana ndi kukula kwa anao komaso kuthekera kwao. Maphunzirowa akhoza kuperekedwa kwa munthu aliyense posatengera zaka. Kuonjzera apo, maphunzirowa alinso ndi mawu ozama (mawu oti tiwadziwe) komanso ntchito zosiyanasiyana zomwe zimapindulitsa nthawi yanu ya maphunzirowa. Kukhala ndi dimba kapena kusamalira zomera zodzalidwa mmiphika ndi kopindulitsa makamaka kwa mwana.

Zigawo za zomera





Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

Tingakule Bwanji Mwa Ambuye?

A. Kuunika Mutuwu Mwachidule

1. Fanizo la Wofesa (Mateyu 13: 1-17)

Mitundu inayi ya nthaka

nthaka yabwino, nthaka ya minga, nthaka ya m'mbali mwa njira, nthaka ya miyala

2. Nthaka ya m'mbali mwanjira

Nthaka yolimba

yokwanira payokha

Nthaka yong'ambika

kugonja

3. Mbewu yofesedwa paminga

Mbewu yoipa

kudetsedwa

Mbewu yabwino

chiyero

4. Wofesa (pa nthaka ya miyala _ntchito yakuthupi)

Nthaka yosalimidwa

ulesi pantchito

Nthaka yolimidwa

kulimbikira kugwira ntchito

5. Nyengo (Ntchito yakuuzimu)

Nthaka youma

Kupanda chikhulupiro (kukaikira)

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

How to Grow in the Lord Lesson2 Outline



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

Nthaka yachinyonho

chikhulupiro (kudalira)

6. Chipatso chanyengo

Chipatso choipa

ntchito zoipa

Chipatso chabwino

ntchito zabwino

Tingakule Bwanji Mwa Ambuye?

GAWO A

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

How to Grow in the Lord Lesson2 Outline



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

(Umoyo wa zomera)

Phunziro 1: Kuunika mwachidule

1. Werengani “Fanizo la Wofesa” lomwe likupezeka m’buku la Mateyu, chaputala 13. Nkhani yabwino kwa ana yomwe ikhoza kugwiritsidwa ntchito m’ malo mwake kapena kuphatikizira pa nkhanayi ya m’buku la Mateyu ndi nkhanayi ya “Mbewu zomwe zinakula ndi kubala zana” yolembedwa ndi Victor Mann (Arch Books; Concordial Publishing House)
2. Kambiranani ndi ana anu tanthauzo la mawu akuti “fanizo” komanso kusiyana pakati pa zinthu za kuthupi (zomwe zingathe kuoneka ndi maso) ndi zinthu zakuuzimu (zomwe sizioneke ndi maso). Fotokozani kuti anthu okhawa omwe akuyenda ndi Ambuye adzakhala ndi kuthekera komvetsetsa zinthu zauzimu.
3. Perekani chiyambi cha ndondomeka ya “Tingakule Bwanji Mwa Ambuye?” Ichi ndi chithunzi choothandizira ndipo chiyenera chilekanitsidwe ndi bukuli ndi kuikidwa malo oonekera bwino. Chithunzichi chizingwiritsidwa ntchito pofotokozera phunziro lonseli. (Chiyambi cha ndondomekoy chikhoza kugwiritsidwa ntchito kwa ana aang’ono pophunzitsa chiyambi cha kukula mu uzimu- kumva, kuchita, ndi kugawana).
4. Pogwiritsa ntchito tchati, fotokozani Magawo asanu a kakulidwe ka zomera:
 - A. Nthaka- pansi kapena dothi, malo okulirapo
 - B. Mbewu- gwerokapena chiyambi cha zomera
 - C. Wofesa- wosamalira
 - D. Nyengo- ndondomeko ya nyengo (mvula, chilala, kutentha, mphepo)
 - E. Chipatso cha nyengo- mbewu, zipatso zake, zokolola

Khalani ndi nthawi younikiranso bwino gawo lililonse, kuchokera pa chiyambi cha mbali yakuthupi yokha. Muunikirensa fanizo Iija kuti mudziwe zomwe Yesu adanena kuti zidachitika ndi mbewu zomwe zidayesera kuti zikulire mu mitundu inayi ija ya nthaka (nthaka ya miyala, nthaka yaminga, nthaka ya m’mbali mwanjira ndi nthaka yabwino).

Phunziro 1: Ntchito

Kukhala Wofesa

Lolani ana anu kuti afese ndi kusamalira mbewu pawokha.

- Zinthu zofunika kukhala nazo:**
- a, miphika yaing’ono inayi ya maluwa
 - b, paketi imodzi ya mbewu(monga zitheba, nyemba)
 - c, dothi
 - njere za mtundu ulionse wa tchire lam’ munda timiyala



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

zibuma (gulumwa) lolimba

Zoti muchite: Pamene mukupitilirabe kukamba nkhani ya “Wofesa” athandizeni ana anu kubzalamithundu yonse itatu yambewu yomwe yatchulidwa mu fanizo muja.



Good Tengani dothi komanso mbewu yabwino; thirani dothi lokwanira 3 kota mu m’phika ndipo bzalani mbewu ija.



Thorny Tengani dothi, mbewu yabwino komanso njere zochuluka za tchire lam’ munda; sakanizani mbewu yabwino ija ndi njere zochuluka zija za tchire lam’ munda ndipo muzibzale pamodzi.



Wayside Tengani buma (gulumwa) lolimba lija komanso mbewu yabwino; popanda kuphwanya buma (gulumwa) lija, ponyani mbewu ija pamwamba pake.



Rocky Tengani timiyala, dothi, komanso mbewu yabwino; ikani timiyala tokwana theka la m’phika. Thirani dothi lochepa pamwamba pake kenako bzalani mbewu ija.

Khazikitsani nthawi yoti ana anuwo azithirira komanso kuika mbewu iliyonse pa dzuwa. Aloleni anawa akhale “ofesa” kwa masabata ochuluka omwe ali nkudza. Fotokozani kuti miphekayi itakidwa panja, mbalame zikhoza kubwera ndikudya mbewu zam’mbali mwanjira zija chifukwa chakuti mbewuzo sizidalowe m’kati mwadothi lija. Mukhoza kusiya m’phika wa mbewuyi pamja kuti muone zomwe zingachitike.

Makolo: Ili ndi phunziro lamphamvu lauzimu choncho muyenera kuyamba kupempherera kukula kwa kwa mbewu iliyonse (monga mwa mawu a Mulungu) ndikuti Mulungu atamandike mu nthawi yonse ya phunziroli. Pemphererani vumbulutso pa momwe munga mungawaphunzitsire ana anu choonadi cha uzimu.

- ☐ Sankhani mbewu yomwe ingayambe maluwa mwachangu nkuyamba kubala zipatso pakati pa masabata awiri ndi anayi.



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures


Tingakule Bwanji Mwa Ambuye?

Phunziro 2 Mwachidule

Nthaka ya m'mbali mwa njira

Ntaka yolimba/Nthaka yofewa

- A) Zomwe zikufanana pakati pa i
- B) kufananitsa nthaka yyolimba ndi nthaka yofewa
- C) Kulima_ njira yothana ndi nthaka yolimba
- D) Phindu la nthaka yofewa komanso yosweka
- E) zifukwa zimene anthu ena amalangidwira: Nthaka yolimba
- F) Kubzala pa nthaka yolimba ndi nthaka yofewa
- G) Chidule





Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

Nthaka

Nthaka yolimba/ Nthaka yofewa

chidwi cha uzimu: mtima wamunthu

chidwi cha sayansi: nthaka yabwino kubzalapo

Mawu oyenera kudziwa

nthaka


kudzichepetsa

kusachedwa kusweka

kulima

kudzipereka (kugonja)

kukana



Nthaka inalengedwa ndi Mulungu pa tsiku lachitatu. Munthu analengedwa kuchoka ku nthaka pa tsiku la chisanu ndi limodzi. Mulungu amati mtima wa munthu uli ngati nthaka (Yeremiya 4:3-4, Hoseya 10:12) chifukwa mtima wamunthu ndi wolimba kapena wofewa. Ngati mtima wa munthu nuli wolimba, uyenera “ulimidwe” kuti mtimawo ulandire mawu a Mulungu.

Kufanana kwa Nthaka Yolimba ndi Nthaka Yofewa (Zizindikiro zake)

Kulimba:

Chinthu chimene sichingasinthidwe kapena kukonzedwa kukhala ndi maonekedwe ena.

Icho chimakhala cholimba komanso sichigonjera pomwe chakhudzidwa. Zinthu zolimba

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

How to Grow in the Lord Lesson2 Outline



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

sizichedwa kusweka (ndiko kuti, zimakhala tizidutsa tambiri pomwe zasweka). Zinthu zolimba zimakana kukakamizidwa.

Kufewa:

Chinthu chomwe chikhonza kusinthidwa kapena kukonzedwa maonekedwe. Icho sichimakana kukhudzidwa. Chinthu chofewa chimadzipereka komanso kunqonjera. Zinthu zofewa zimapindika pamene zagwiridwa.

Kodi mtima wanu ndiwolimba kapena wofewa?

Kulima: Njira yosinthira Nthaka Yolimba

Nthaka yolimba singagwiritsidwe ntchito pobzala, chifukwa siingathe kulandira mbewu. Pakuti nthakayi siili yodzipereka, Mu ulimi muli njira zopangira nthaka kuti ikhale yofewa isanadzalidwe mbewu. Njira yogwiritsira ntchito pofewetsa nthaka imatengera mulingo wa kalimbidwe ka nthakayo, nthaka yolimba kwambili imafewetsedwa poigamula, zida zogamura nthakayi zimayenera kukhala zamphanvu komaso zopangidwa kuchekera ku zitsulo zolimba kwambiri. Pomwe chitsulo chamenya nthakai, nthakai imasweka niifewa, izi zimachitika chifukwa chitsulo ndi cholimba kuposa nthaka, ndipo nthaka imakhala yopanda chisankho koposa kudzipereka.

Ngati mtima wathu uli olimba, Mulungu wayenera kuupanga kuti ukhale ofewa kuti utha kunva komaso kulandira malangizo. Kodi mulungu angaufewetse bwanji mtimau? Ndi khasu la chitsulo? kapena piki?

Ubwuno wa nthaka yofewa.

Nthaka yofewa imakulitsa mbeu zabwino kufanizira ndi nthaka yilimba, chifukwa njere zikagwera pa nthakayabwino mizu yake imazama munthakamo ndipo imazika mizu. Nthaka yolimba simalora mbeu kuti zizike mizu chifukwa ndi yolimba kwambiri, mbeuyimakhilabe pamwamba pa nthaka youmai siimamera, pakuiti mbeu siingamere kapena kuphukira. (Yohane 12:24)

Chifukwa chomwe anthu amalangidwira: nthaka yolimba

Hoseya 10:10-12. Mulungu anatomiza anthu ena kuti akagamule Samaria, pakuti Samariamamvetsera kwa Mulungu, anthu awa anatomizidwa kuti akafewetse Samaria.

Ngati sunvera Mulungu nthaka ya mtima wako imakhala yolimba, Mulungu amatha kugwiritsa ntchito makolo ako kuti afewetse nthaka ya mtima wako, ndipo nthawi zina zimapweteka ndithu, kodi mungafotokoze chifukwa chani?

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

How to Grow in the Lord Lesson2 Outline



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

Kodi ndi njira zina ziti zomwe Mulungu amagwiritsa ntchito makolo athu kuti agamule kulimba kwa mtima wathu.

Anthu ena amanva ndi malangizo a pakamwa chabe, ndipo Mulungu amawatcha anthuwa anzeru. (werengani Miyambo 17:10) Anthu ena amanva pokhapokha choipa chiwagwere, (ndodo ya malangizo). Mulungu amati anthu otere ndi opusa. Ndipo anthu ena samanva ngakhale pakutha pa malangizo osalekeza, (werengani Miyambo 27:22) Mulungu akuti anthu oterewa adzasweka modzidzimutsa (Miyambo 29;1)

Kudzala pa nthaka yolimba ndi yofewa

Tadzala kale mbeu zathu mu nthaka yolimba ndi yofewa, kodi inu mukuganiza chingachitike ndi chani. Mateyu 13 akunena juti nthaka ya m'mbali mwa njira siimatha kulandira mbeu, koma mnbeuyo imakhala pamwamba pa nthakayi kufikira mbalame zitaidya, Ndi chifukwa chani nthaka ya m'mbali mwa njira imakhala yolimba (gulu la anthu omwe amadutsa pamwamba pake) nanga Mbalame zikuimira chani? Ndichifukwa chani mbalame (satana) akufuna ku kudya mbeuzi.

Nkhaniyi mwachudule: tayenera kukhala ndi nthaka yofewa kuti mbeu zikule. Tisamakanize chiphuzitso cha ambuye

Pempherani kuti nambuye apereke mtima odzipereka kwa iye

Phunziro #2 chochitika

kufewetsa nthaka

aloleni ana (ophunzira) kuti ayesere kufewetsa nthaka pogwiritsa nthchito njira zosiyana siyana.



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

Zinthu zofunikira: Ma gulumwa a nthaka yolimba.

Timitengo

Shovelo

Madzi

Cholemba

Zoyenera kuchita: Tengani timitengo tija kuti muyese kalimbidwe ka zigulumwa za nthaka yolimba ija.

Uzani ophuzira anu aliyese atenge kamntengo nayese kuti ayiboole nthaka ija ndipo ayese kuya kwake, ndipo alembe mzera pansu pa mbali yomwe siinalowe mu nthaka. Kukula kwa mtengo mbali yomwe ikuonekera ikuonetsera kulimba kwa nthakayo ndipo ndi yosagongera. Muchotse kamtengo kaja ndi kuithira madzi nthakayo ndipo muyesenso kukanikiza ka mtengo kaja mu nthaka ija, lemani nzera pa pomwe ntengo waleka kulowa mu nthaka ndipo mutha kudziwa kuti nthakayo ikufewa kapena ayi. Ndipo tsopano gwilitsani ntchito chida cholimbirapo ndi cha mphanvu kuti muswe nthakai, kenako yesaniso ndi kandodo kaja. Afuseni ana omwe mukuwaphunzitsa kuti kodi ndi nthaka iti yomwe ingalandire mbeu nanga ndi chifukwa chani ingateero.

Mu nthawi ya chochitika ichi muonrtsetse kuti mwalankhula ndi ophunzira anu zokhudza mtima wao ndi momwe Mulungu amafunira kuti mitimayo ikhale yofewa kwa iye, auzeni ophunzirawo kuti Mulungu amawakonda kwqambiri ndi kuti adzapitiriza kugwiritsa ntchito makolo ndianthu ena kuti afewetse mitima ndi cholinga choti atha kulandira mau ake (malangizo) ndi kumakula.

.....Pothera pa Gawo loyamba.....

Mmene Mungakulire Mwa Ambuye Phunziro 3


Kulongosola Mbewu (Minga)

Mbeu Yoipa/Mbeu Yabwino

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

How to Grow in the Lord Lesson 2 Outline

Page 13





Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

- A. Mbewu Zoyipa ndi Zogulitsa Zabwino
- B. Zoyambira Zoyipa ndi Kufalitsa
- C. Kuloweza: Kuika Mbeu Yabwino
- D. Kuzindikira Mbewu Yoipa ndi Mbewu YabwinoKuwala / Mdimu
- E. Mawu a Mulungu ndi Kuwala
- F. Chidule

MBEU

Mbeu Yoipa/Mbeu Yabwino

chindunji cha uzimu: Mau a mulungu ndi mbeu yabwin, kuzindikira zabwino ndi zoipa

chindunji cha sayansi: Mitundu ya mbeu, kufesa mbeu

Mau oyenera kudziwa

Mbeu	zindikira
Maudzu	tchimo
kuyera	kuunika
kudetsedwa	mdima
kufalitsa	zotsatira





Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

(*tanthauzo lakuthupi ndi lauzimu)

Zotsatira za Mbewu Zoyipa ndi mbewu Zabwino

Pali mitundu yambiri ya mbewu. Asanabzale, mlimi ayenera kusamala kuti aone ngati mbewu zake ndi zabwino. Mbewu zabwino zimabala zipatso zabwino. Mbeu zoyipa zimabala zipatso zoyipa. Alimi amabzala mbewu zabwino chifukwa chofuna kubala zipatso zabwino. Zipatso ndi ndiwo zamasamba ndi mbewu zabwino. Udzu ndi dongosolo lililonse la mbeu zosafunidwa zomwe zimakula mochuluka kutsekereza mbewu yomwe mukufuna, nthula ndi mitungwi onsewa ndi mitundu ya udzu. Izi sizili chinachake chimene mukufuna kudya. Izi zimakoma moyipa.

Nthaka yaminga: Kochokera ndi kokulira njere zoyipa

Nthaka iliyonse yomwe siyang'aniridwa, imakhala ndi mewa zoipa. Kamba koti njere zoipa zimafala mmalo osiyanasiyana ndi mphepo komanso udzu wina. Ndipo ndondomeko iyi ndiyo kuchulukitsa (kukwatitsa). Mukaona munda kunjako, muona kuti mbewu zoyipa zimakulanso paliponse ngakhale opanda wina kuzibzala kapena kuziyang'anira. Udzu umafinya mbewu zabwino mukazilekerera.

Kuloweza: Kuika njere zabwino

Baibulo limati tonse tinachimwa ndikuperewera pa ulemerero wa Mulungu (Aroma 3:23). Kuchimwa ndi kupanga zomwe Mulungu kapena Mawu ake anatiletsa. Anthu tonse tinabadwira mu uchimo. Ngati mtima wanu suyang'aniridwa (posawulima ndi kubzalamo) mtima wanu upitilira kukura mu uchimo (udzu) monga mmene muonera minda yakunjayi.

Mawu a Mulungu ndi njere yabwino, amatipangitsa kumaganiza maganizo abwino. Izi zimabereka zipatso zabwino. Mulungu afuna tiloweze mawu ake ndipo kuti tikwanitse tiyenrra tifewetse mitima yathu.

Monga minda, udzu (njere zoyipa) zimabwera kuchokera kulikonse kuti zifinye mbewu zabwino. Abwenzi oyipa, Makanema komanso maganizo oyipa anu omwe ndi udzu. Ngati mumva ndi kulandira (monga dothi lofewa) Malangioz a Mulungu ndikuchita zomwe Anena, mudzakula ndikubereka zipatso zabwino.

Kuzindikira Mbewu Yoipa ndi Mbewu Yabwino

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

How to Grow in the Lord Lesson2 Outline



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

Nthawi zambiri mbewu yabwino imasakanikira ndo mbewu yoyipa. Izi nzimene zinachitika ku mbewu yapaminga mu “Fanizo la ofesa mbewu”. Pamene mbewu zonse zimakulira limodzi, mbewu yoyipa ija inafinya mbewu yabwino. Nthaka yake siinali yangwiro. Mawu oti ungwiro imatanthauza kusamalika, yosasakanikirana, yopanda zilizonse zodetsa. Mbewu yomwe yabzalidwa limodzi ndi njere zina zosiyana (kapena nthaka yomwe inali ndi njere zina kale) imabweretsa mbewu zosakanikira.

Kodi ungasiziwe bwani njere zabwino kuchoka ku njere zoipa? Kodi ungasiziwe pakungoona basi? Pakumva fungo? Pakugwira?

Njira imodzi yodziwira njere yabwino ndiko kudziwa komwe ichokera. Njere zabwino zimachokera ku zipatso zabwino. Njere zoipa zimachokera ku zipatso zoipa. Mukacheka oranje ndikutenga njere zake nkuzibzala mudzakolora oranje. (Werengani Mateyu 7:16-20).

Mawu a Mulungu ndi angwiro. Siwosakanikirana ndi chilichonse. Mukabzala mawu oyera a Mulungu, mudzabala zotsatira zoyera.

Njira ina ndikyo kuziyang’anira pomwe pakuwala. Alimi ambiri amaona njere, pamalo pomwe pali kuunika kwabwino, ndikudziwa zomwe njere ija idzabereke. Atakhala kuti waphimbiwa mmaso, njerezo zitha kukhala kovuta kuzisiyanitsa. Yohane 9:4,5 akuti tikuyenera tigwire ntchito kunakayera (kukuwala)...popeza ukudza usiku omwe aliyense sangagwire ntchito. Alimi amagwira ntchito masana kutik ziwona.

MAWU A MULUNGU NDIWO KUWUNIKA

Baibulo ndiwo muuni wathu odtidziwitsa mbewu zabwino ku zoipa. Masalimo 119:11 akuji “Ndasunga mawu anu mumtima kuti ndisakuchimwiren” tifunika kuunika kuti tikwone.

Mawu a Mulungu ndiye kuunika komwe kumatithandiza kusiyanyitsa chabwino ndi choipa. Popanda kuunika tili mumtima. Zili ngati kuti taphimbidwa mmaso. Popeza Mawu a Mulungu ndi angwiro, tili ndikukhulupiliro kuti chilichonse chomwe chili mu Baibulo chimatitsogolera ku zinthu zokhazo zomwe zili zabwino. Yesu anati “Ine ndine kuunika kwa padziko”.

Mwachidule :

- ☐ Mawu a Mulungu ndi oyera. Osawonjezera china chirichonse kwa izo.
- ☐ Mawu a Mulungu ndi kuunika kumene kumatithandiza kusiyanyitsa chabwino ndi choipa.

Onetsetsani kuti mbeu zonse zomwe mwabzala mu mtima mwanu ndi zoyera!!



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

Phunziro #3: Zochitika

Kuzindikira Mbewu

Kodi mutha kusiyantsa mbewu yabwino ndi yoyipa popanda kuwala, kapena popanda kudziwa kumene idachokera?

Zomwe mungafunikire:

- ☐ Mbewu zosiyanasiyana (zabwino ndi zoyipa zomwe)
- ☐ Chotchinjilizira mmaso
- ☐ Kuwala
- ☐ Zipatso zosiyanasiyana zomwe zili ndi njere zoonekera
- ☐ Udzu osiyanasiyana omwe uli ndi njere zowonekera

Zomwe mungachite

1. Dulani chipatso chilichonse (ie apulo kapena lalanje) ndikuchotsamo njere. Yoyolani njere za udzu omwe ulipo. Njere iliyonse ikhkale pamene pali chipatso chake, afunzeni ana kuti anene njere zomwe zili zabwino komanso zoyipa. Gwiritsani ntchito izi pofotokoza chifukwa chomwe Yesu ankati Mtengo uliwonse umadziwika ndi zipatso zake kuti uwu ndiwabwino kapena ayi.
2. Gwiritsani ntchito chopimba m'maso kuti mutseke kuwala kwa maso a mwana wanu. Ikani mbeu zingapo patebulo (ngati pali ana ambiri ikani njerezo m'thumba la mapepala kuti ana ena asaone). Yesani kugwiritsa ntchito njere zomwe mwana wanu amazidziwa bwino. Lolani mwana wanu kuti adziwe kuti mbewuyo idachokera kuti pakuzigwira. Kodi ndi mbewu yabwino kapena yoyipa? Tsopano chotsani chotchinga m'maso ndi kulola mwana wanu kuti awone njerezo. Kodi zinathandiza kusiyantsa mitundu iwiri ya mbewu? Lankhulani ndi mwana wanu za Yesu yemwe ndi kuwala kumene kumatithandiza kuona. Popanda lye n'kosatheka kusiyantsa chabwino ndi choipa kapena zinthu zina za uzimu (monga mafanizo).




Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

Kodi Mungakule Bwanji Mwa Ambuye

Phunziro #4: Ndongomeko

Ofesa (Miyala-Kugwira ntchito)

Nthaka yosalimidwa/ nthaka yolimidwa



WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

How to Grow in the Lord Lesson 2 Outline



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

Ulesi/ kulimbikira

- A. Ntchito ya Adamu: Tsogolo la munthu
- B. Kugwira ntchito molimbika ndi kovuta
- C. Chifukwa chiyani wofesa ayenera kukhala wakhama
- D. Wofesa waulesi amapeza njira “yosavuta” yotulukira: Dothi lamwala
- E. Malizani ntchito ya Ambuye.

Wofesa

Nthaka yosalimidwa/ Nthaka yolimidwa

Ku uzimu tiona: Kusiyanitsa kwa ulesi ndi khama

Ku Sayansi tiona: Kulima nthaka; mmene mbewu zimapezera chakudya

Mawu Oyenera Kuwadziwa

Ofesa


Kulima

Khama

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

How to Grow in the Lord Lesson2 Outline

Page 19





Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

Ulesi

Mizu

Kumera mizu

Ntchito ya Adamu: Tsogolo la Munthu

Adamu anapangidwa kuchokera ku dothi kuti avale ndi kusunga Munda wa Edeni. Adamu atachimwa, anauzidwa kuti nthaka yake idzamera minga ndi mitula. (Kodi nthula n'chiyani?) Koma ngati Adamu anagwira ntchito mwakhama, akanathanso kulima zitsamba m'nthaka yake. (Onani Gen 3:18). Adamu anayenera kukhala wofesa mbewu, mlimi ndi woyang'anira.

Kulimbikira Ntchito Ndikovuta Komanso Yokhumudwitsa

Kugwira ntchito mmunda yokuza mbewu ndi ntchito yolimba. Pali zinthu zambiri zomwe zingawononge ntchito zonse zomwe mungagwire m'munda mwanu. Udzu, tizilombo ndi mbalame zonse zili ndi njira yoletsera mbewu zabwino kumera. Miyala pansu pa nthaka imalepheretsa mizu ya mbewu kukula. (Yesaya 5:1-2). Nthaka yathu iyenera kupwanyidwa kwambiri kuti mizu izikula.

Chifukwa Chani Wofesa Ayenera Kukhala Wakhama

Ngati wofesayo sali wakhama, ndipo osagwiritsa ntchito mwanzeru nthawi yake kugwira ntchito ndi kusamalira mbewu zake, mbewu zake zimafa. Mbewu zake zizingapulumuke chifukwa nthaka sinakonzeka kuti mumere mbewu. Kusamalira nthaka nthawi ndi nthawi ndikofunikira. Njira yosamalira nthakayi ndiyo imatchedwa kulima. Mlimi sangangothira njere m'nthaka kenako n'kugona mpaka zipatso zitamera m'munda mwake. Ayenera kuthirira komanso kuonetsetsa kuti ndi yopanda udzu, nsikidzi ndi tizirombo tina.

Mu "Fanizo la Wofesa," mbewu zimene zinagwera pamiyala zinamera mizu ndipo nthawi yomweyo zinayamba kukula. Chomeracho chinkaoneka chathanzi, koma pasanapite nthawi yaitali, mbewuyo inayamba kufa. Izi zinachitika chifukwa panali miyala pansu pa nthaka yomwe sinachotsedwe mbewuyo isanabzalidwe. Mizu ya chomeracho pamene inkapita pansu, miyalayo inkalepheretsa kuti isalowe. Chomera chokhala ndi mizu siyozama sichikhalitsa.

Mizu ndiyo imadyetsa ndi kulimbikitsa zomera. Zimalowa pansu m'nthaka kutunga madzi ndi zakudya pansu pa nthaka n'kuzisunga. Mizu imalgwira chomera ndikulora kuti chizikula mwamphamvu. Mizu yolimba ndiyofunikira kuti zomera zizilimba. Ngati mizu ya chomera yasiya kukula chomeracho chimasiyaso kukula.

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

How to Grow in the Lord Lesson 2 Outline



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

Momwemonso, sitingangowerenga ndi kuloweza malemba (mbewu ya Mulungu) ndi kuyembekezera kuchita zodabwitsa kwa Ambuye. Baibulo limati mu Yakobo 1:22 tiyenera kukhala akumva ndi akuchita (olima) Mau. Pali zinthu zambiri zimene tiyenera kuchita kuti munda wa mtima wathu ukhale kwa Yehova. Tiyenera kufufuza miyala ndi tizilombo m'munda mwathu kupand kutero mbewu zathu zambiri zitha kufa.

Kodi ndi miyala kapena tizilombo titi tomwe tikulepheretsa mizu yanu yauzimu kukula?

Mutu wa Phunziro

Miyala ndi Tizilombo

Nthaka

Kuumitsa mtima

Njere

Abwezi oipa, Malingaliro oipa

Ofesa

Ulesi

Nyengo

Mantha/ Kusakhulupilira

Chipatso

Zochita zoipa (Udzu)

Wofesa Waulesi amapeza njira “zachidule” (Sachita zinthu mwadongosolo)

Wofesa Waulesi amaona kuti ndi dothi lapamwamba lokha lomwe ndilofunika kuilimidwa, choncho amangokonza gawo la dothi limene anthu amaona. Koma, dothi ndi lolimba mkati nalonso. Ngakhale titagwira ntchito molimbika bwanji, nthawi zonse pamakhala chinthu china choti tikonze m'mundamo.

M'mitima yathu, timaganiza kuti Baibulo siligwira ntchito pa mbali iriyonse ya moyo wathu, kapena kuti nzovuta kwambiri kuchita ntchito yofunika kuchitidwa. Zotsatira zake, timangokonza gawo la mtima wathu lomwe anthu atha kuwona. Timapita kutchalitchi Lamulungu, ndikuyiwala za Mulungu mkati mwa sabata yonse. Timangonyalanyaza zimene Yehova watiuza tikamva zinthu zimene zimawoneka zovuta kuzichita.

”ndinkayenda mmbali mwa munda wa munthu waulesi, ndinadutsa mmunda wa mphesa wa munthu opanda nzeru ndinapeza kuti paliponse mmundamo pamera minga, mnthaka imeneyo munali mutamera nkhwisa ndipo mpanda wake wamiyala unali utawonongeka. Tsono nditaona ndinayamba kuganizira mumtima mwanga ndipo ndinatolapo phunziro ili: ukati bwanji ndigoneko pang'ono kapena ndiwodzereko pang'ono kapenanso ndipindeko manja pang'ono kuti ndipumule, umphawi udzafika pa iwe ngati mbala ndipo usiwa udzakupiza ngat munthu wachifwamba.” Miyambo 24:30-34.

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

How to Grow in the Lord Lesson 2 Outline



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

Wofesa waulesi amakuganiza kuti amapulumsa thukuta, ululu, ndi kuvutika kwake chifukwa sanavutikire kugwira ntchito zolimba kuti apeze miyala ndi tizirombo mmunda wake. Komatu pomwe dzuwa lidzawala kuti likulitse mbewu adzazindikira kuti sanachite gawo lake ndipo zomera zake zidzafa. Adzakhala opanda mbewu.

Ngati tikhala aulesi, tikuba nthawi imene Yehova watipatsa kuti tibzale mbewu zabwino. Ngati tiika Yehova pamwamba pa mitima yathu, mizu yathu sichitha kuzama ndipo mbewu zathu sizidzakula mwamphamvu.

Mwachidule

Tikuyenera kukhala a khama ndi olimbika pa chilichonse chomwe Yehova watiuza kuti tichite.

Osalola kuti miyala ndi tizirombo zipangitse chomera chanu chisakule!!!

Phunziro #4 Chochitika

Chomera chopanda mizu yozama

Bzalani chomera poti mizu siizama kuti muonetse mmene zimakhallira ngati mizu siikukula.

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

How to Grow in the Lord Lesson2 Outline



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

Zomwe mungafunikire:

- ☐ Chisusu (siponji)
- ☐ Njere iliyonse yomwe imamera mwachangu (monga nyemba yomera kale)
- ☐ Madzi

Zoyenera kuchita:

Ikani njere zambiri mu siponji, iviikeni siponji ija mmadzi. Ikani siponji ija padzuwa. Onetsetsani kuti siponji ija izikhala ndichinyonho. Mwakanthawi njere zija ziyamba kuphukira. Kenako zimafa. Kodi mukudziwa chifukwa chake? Izitu nchifukwa chakuti siponji simalora kuti zomera zizimera mizu. Ichi ndichitsanzo cha nthaka ya miyala. Ngati chomera chilibe mizu, sichingakule.

Iyi ndi nthawi yabwino yokambirana ndi ana anu kuti musamafune zotsatira zachangu nthawi zonse. Chinthu chabwino chimatenga nthawi kuti chipangidwe ndipo chimafuna khama lalikulu. Zotsatira inde ndizofunika. Nthawi zina pamene zinthu zachitika mofulumira kwambiri, mphanvu zanu zimapita pachabe chifukwa zotsatira zake sizikhalitsa.

Lolani mwana wanu kuti azigwira ntchito mwakhama payekha. Asunge munda (wanu kapena oyandikana nawo) opanda udzu kwa sabata imodzi kapena ziwiri. Muyanikireni kapena kumpatsa mphoto chifukwa cha khama lake.



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

Tingakule Bwanji Mwa Ambuye

Phunziro #5 Ndongomeko Yake

Nyengo (Ntchito Za Ku Uzimu)

Dothi Louma/ Dothi Lonyowa

(kukayikira) (chikhulupiriro)

A. Gawo la Ambuye pakukula kwa mbewu

B. Chitsamba chouma; mtengo wothirira

(mchipululu) (pakasupe)

C. Chifukwa chiyani kudalira Yehova kuli kofunika?

D. Kusinkhasinkha: Kulingalira za Ambuye

Davide ndi Goliati

Mkango ndi Chimbangondo





Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures
Kukumbukira Yehova

Nyengo

Dothi Louma/ Nthaka yonyowa

Kuuzimu tiona: Chikhulupiliro, kudalira mwa Mulungu

Ku sayabsi tiona: Mmene nyengo zimasinthira

Mmene madi amapangikira

Nyengo

Mmene zomera zimapangira chakudya



Mawu oyenera kuwadziwa

Nyengo

Chikhulupiliro

Kudalira

Kasupe

Kumera

M'phunziro lapita, wofesa waulesi sanachite chilichonse chimene Yehova anamuza kuti achite. Mu phunziro ili, wofesayo amanyengedwa kuti iye amachita chilichonse kuti mbewuyo ikule ndipo Yehova sachita chilichonse kuti mbewuyo ikule.



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

Pakukula kwa mbewu, munthu amakhala ndi gawo lake (wofesa) ndipo Yehova ali ndi gawo lake.

Gawo la Ambuye pa Kukula kwa Zomera

Ambuye amapangitsa mbewu kumera (kuyamba kumera, kuphukira) ndi kukula. Iye amapereka madzi ku zomera. Iye amatipasa zinthu zonse zomwe tibafuna mnthawi yake.

Mmene Ambuye anakonzera

“Umu ndi mmene ulili ufumu wa Kumwamba. Munthu amafesa mbewu mnthaka. Usiku ndi usana, kaya agona kaya adzuka mbewu imamera ndi kukula, ngakhale sadziwa mmene zimachiikira. Nthaka payokha imatulutsa mbewu, umayamba mmera kenaka ngala, kenaka mbewu yakhwima mngalayo. Mbewuyo ikangokhwima, amayimweta chifukwa nthawi yokolora yakwana. Maliko 4:26-29.

Pali zinthu zambiri zomwe mbewu zimafunikira kuti zikule zomwe mlimi sangathe kuzikonza. Zonse zili mdzanja la Ambuye. Nyengo ndi yofunika kwambiri ku chomera. Nyengo ndi momwe mlengalenga ulili monga kutentha, chinyontho kapena mitambo. Nyengo zimasintha nthawi zonse chaka chonse. Monga malo asiyana mmene ayandikilira dzuwa, nyengo zosiyanasiyana zimabwera. Mlimi amayenera adziwe nyengo yoyenera kubzala njere zake.

Yehova anaikanso dzuwa kumwamba (pa tsiku lachinayi). Zomera zonse (ndi nyama) zimafuna kuwala kuti zizikula. Zomera zambiri zimagwiritsa ntchito kuwala kwa dzuwa kupanga zakudya zake (photosynthesis). Munthu amazitenga mopepuka kuti dzuwa limawala tsiku ndi tsiku ndikupereka kuwala ku zomera zake.

Poopeza mvula imagwa kuchokera kumwamba kuthirira nthaka ndipo pamapeto pake imabwereranso kumwamba (mmene madzi amapangidwira) ndi chinsinsi china chimene munthu akuganiza kuti chidzapitirira kuchitika. Mulungu ndi wokhulupirika. Tikhoza kudalira pa Iye (kukhulupirira) kuti apangitse dzuwa kutuluka, mvula kugwa ndi mbewu kumera. Iye adzachita gawo lake.

Chitsamba chouma/ Kasupe wamadzi

Tikamaganiza kuti tikhoza kuchita zinthu popanda Mulungu timavutika ndi chilala. Chilala ndi pamene chomera sichilandira madzi kwa nthawi yaitali. Izi zimachitika nthawi zambiri m'chipululu komanso m'nyengo yotentha. Malo amene kuli kasupe wa madzi ndi osiyana ndi chilala. Ndi malo achonde m'chipululu chifukwa cha madzi. Izi ndi zimene Baibulo limanena pa Yeremiya 17:5-8.

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

How to Grow in the Lord Lesson2 Outline



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

Chilala

Ndiwotembererdwa munthu amene amadalira munthu mzake, amene amatsamira mzake kuti amuthandize pamene mtima wake wafulatira Yehova. Munthuyo adzakhala ngati chitsamba cha mchipululu mopanda madzi dziko la mchere limene munthu sangathe kukhalamo. Ali mu nthaka yotentha ndo youma yomwe ili yoyipa. Sadziwa za ubwino komanso zabwino zomwe Mulungu amatha kupereka.

Kasupe

Koma wodala munthu amene amadalira Yehova, amene amatsamira pa Iye. Adzakhala ngati mtengo wodzalidwa mphepete mwa madzi umene umatambalitsa mizu yake mmballi mwa mtsinje, mtengowu suopa kutentha; masamba ake amakhala obiriwira nthawi zonse sachita mantha pa chaka cha chilala ndipo sulphera kuberek zipatso.

Tajambulani zithunzi ziwiri zosonyeza nyengozi.

Chifukwa chiyani Kudalira Mulungu Nkofunikira

Tikadalira Yehova, timakhala olimba chifukwa Iye amatidyetsa. Kodi Yehova amatidyetsa bwanji? (Onani Masalimo 1:3, Yereimiya 17:8 ndi Deutoronomo 11:14)

Nthaka youma ilibe madzi chifukwa wofesa amaganiza kuti mphamvu zake zimachokera kwa iye yekha osati kwa Mulungu. Mizu yake sipeza madzi chifukwa amadalira nthaka yake. Koma Yehova ndiye Madzi athu (Yohane 4:14).

Kusinkhasinkha: Kuganizira Mawu a Mulungu.

Nthawi zonse tizidalira Mulungu. Timaphunzira kudalira Mulungu pomwe tikumuganizira Iye ndi kuona dzanja lake pa ife. Salimo 1:2-3 limanena kuti tidzalandira mphoto ngati tisinkhasinkha pa Mawu a Mulungu. Kusinkhasinkha Mawu a Mulungu kumatanthauza kukhala ndi chithunzithunzi ndi kuona m'maganizo zimene Mulungu amanena m'Baibulo. Iye amatipangitsa ife kukumbukira pomwe adatithandiza.

Kodi mukukumbukira pamene Davide anali pafupi kumenyana ndi Goliati? Davide anakumbukira pamene Mulungu anamuthandiza kugonjetsa mkango ndi chimbalangondo m'mbuyomo. Kukumbukira zimenezi kunam'patsa kulimba mtima (mphamvu) kuti amenyane ndi Goliati wa ku Gati. Tikamakumbukira "sabata" (lamulo lachinayi), tingapumule mwa Yehova chifukwa ndi wokhulupirika kuti atithandize.



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

Mulungu ndi wokhulupirika monga momwe dzuwa limatuluka kuchokera kum'mawa kupita kumadzulo. Ndipo ngakahale mitambo itaphimba dzuwa masana, sizitanthauza kuti dzuwa lo palibe ayi; chimodzimodzinso, ngakhale sitingathe kumuwona Ambuye (Kuunika kwathu), sizitanthauza kuti lye palibe.

...ndipo popanda chikhulupiliro nkosatheka kukondweretsa Mulungu, chifukwa aliyense amene mabwera kwa lye ayenera kukhulupilira kuti Mulungu alipo ndi kuti lye amapereka mphotho kwa amene akumufunitsitsa. Aheberi 11:6.

Ngati tisinkhasinkha za Ambuye, tsamba la mbewu yathu silifota, ngakhale ena onse adzauma.

Mwachidule

Tiphunzire kudalira Mulungu posinkhasinkha Mawu ake ndipo adzakupatsani mphamvu. Kumbukirani zimene lye amakuchitirani inu.

Phunziro #5 Chochitika

Kupulumutsa Selari (chomera)

Izi zithandizira ana anu kuona mmene mizu imatengera madzi ndikupereka moyo kwa chomera.

Zomwe mungafunikire 1. selari ofota

2. Jagi cha galasi

3. thilirani maulendo ambiri koma m'madzimo muikemo

zoonjizera mtundu



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

Zoyenera kuchita

Musanayambe, lolani mwana wanu kuti ayang'ane phesi la udzu uliwonse omwe unafota. Chifukwa chiyani zili choncho opanda moyo? Kodi ndizothandiza kapena ziyenera kutayidwa? Fotokozani kuti zamoyo zonse zimafunika madzi kuti zikhale ndi moyo. Ichi ndichifukwa chake Mulungu adapanga madzi pa tsiku lachiwiri la chilengedwe asadalenge zomera (tsiku lachitatu), nsomba ndi mbalame (tsiku lachisanu) komanso munthu ndi nyama zokhala panso (tsiku lachisanu ndichimodzi). Iye ankadziwa kufunika kwa madzi. Funsani komwe madzi amachokera. Kodi munthu amapanga madzi?

Ikani udzu wa selari mu mtsuko wa galasi. Lembani ndi madzi openteja. Kupaka utoto kumathandizira mwana wanu kuwona madzi akukwera mu phesi la udzu wa serali uja. Mudzawona zotsatira zofulumira kwambiri mu kaonekedwe ka phesi la serali ukamalandira madzi. Kambiranani za zinthu zonse zimene Mulungu watipatsa ndipo akupitiriza kutipatsa. Kumbukirani zina mwa zokumana nazo za banja lanu pamene Yehova anapereka “madzi” zimenezo zinali zofunika kuti banja lanu likule. Lankhulani kukhulupirika kwa Mulungu kwa inu. Kambiranani chimene madzi amaimira (Yeremiya 2:13; Yohane 7:37).



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

TINGAKULE BWANJI MWA AMBUYE

Phunziro #6 Ndongomeko Yake

Chipatso cha Nyengo

Chipatso chabwino/ Chipatso choyipa

- A. Chifukwa chiyani Chipatso Cha mu nyengo yake?
- B. Kubereka kutengera mtundu wake
- C. Kuchulukitsa Mbewu: Kuchulukitsa Zipatso
- D. Kufananiza pakati pa Chipatso cha Mbewu ndi Makhalidwe Anu.
- E. Mwachidule





Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

Chipatso mu nyengo yake

Chipatso Choyipa / Chipatso Chabwino

- Ku uzimu tiona:** Chipatso chimatengera mtundu wake;
Kugawana chikhulupiliro chanu ndi ena
- Ku sayansi tiona:** Chipatso chimatengera mtundu wake;
Kuchulukitsa mbewu

Mawu oyenera kuwadziwa

- Kukolora
- Kubereka
- Tuta
- Fesa
- Chulukitsa
- Mbewu

Chifukwa chiyani Chipatso mu nyengo yake?

Salimo 1:3 ndi Yeremiya 17:8 amanena kuti tidzabala zipatso m'nyengo yathu. Ngati tisinkhasinkha pa mawu a Mulungu. Mbewu zimabereka zipatso nthawi inayake m'chaka. Ngati chomera sichikubala zipatso, chimakonzekera nyengo ina yobala zipatso. Zimatenga nthawi kuti mbewu zikule ndi kukula mwa Ambuye. Kukula sikungochitika mwadzidzidzi. Zomera zina zimatha kudutsa zaka zambiri zisanabale zipatso. Katsitsumzukwa,

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

How to Grow in the Lord Lesson2 Outline



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

mwachitsanzo, kamatenga zaka ziwiri kuti kadzabereke. Ngati alimi ali oleza mtima ndi kupitiriza kugwira ntchito molimbika, m'kupita kwa nthawi adzapeza zokolola zambiri. Iyi ndi nthawi ya chaka imene mbewu zokhwima zimasonkhanitsidwa. Iyi ndi mphotho ya mlimi pa mphamvu zake zonse. Enanso amapindula kuchoka ku khama la mlimi. Palibe chomwe chimakhutitsa chilakolako monga mokwanira mphesa zakupsa m'dzinja! Ndiwotsekemera komanso abwino kwambiri.

Chimodzimodzinso, palibe chimene chimakhutiritsa moyo mofanana ndi mtumiki wa Ambuye amene akuchita chifuniro cha Yehova. Msamariya Wachifundo (Luka 10:30-37) ndi chitsanzo chimodzi. Kodi mungaganizire zitsanzo zina? Zitha kutenga nthawi, koma ngati mukhala okhulupirika mu zonse zomwe Yehova wakuyitanirani kuti muchite, inunso mudzabala zipatso munyengo yanu!

Kubala Zipatso kumatengera Mtundu Wake

Njere zimene zabzalidwa m'nthaka zimakula n'kukhala chomera chobala zipatso. Mbewu ikafesedwa munthaka, chipatso chomwe cha mbewu yabzalidwacho ndicho chimaberekedwa. Genesis 1:11 akuti mmera uli wonse ubala monga mwa mtundu wake. Izi zikutanthauza kuti ngati mutabzala mbewu ya apulo, idzabweretsa mtengo wa apulosi. Simungabzale njere ya lalanje ndikuyembekeza kutulutsa apulosi.

Agalatiya 6:7, 8 limatiuza mwanjira ina. kuti "... chimene munthu wafesa, chimenenso adzachituta." Kufesa kumatanthauza kubzala mbewu kuti ikule. Pamene kukolola ndikututa mbewu, kapena phindu lolandira monga mphotho ya ntchito yanu.

Ngati mufesa mbewu zoipa, mudzatuta zoipa. Ngati wafesa zipatso zabwino, udzatuta zipatso zabwino ngati mumasamalira chomera chanu ndikuchiteteza ku zinthu zoyipa zomwe zingachitike

Kuchulukitsa Mbewu

Chomera chomwe chikumera chimachulukitsa (kuchulukitsa nambala) mbewu ndikupangitsa kuti kudzakhale kotheke kulima zochuluka za iyo, kaya ndi yabwino kapena yoyipa. Mukadula apulosi, mudzapeza njere zingapo mkati. Mbewu iliyonse ikhoza kubzalidwa kuti pamapeto pake itulutse mtengo wina wa maapulo. Mtengo wa maapulo umenewo udzakhala ndi maapulo ambiri ndi njere zina zingapo mu uliwonse. Amatha kuberekanso maapulo mazana ambiri. Kuchulukitsa (kupanganso) kapena kuchulukitsa ndi njira yomwe imadziwika kuti kufalitsa. Kumbukirani mu phunziro 3 momwe namsongole adawonekera m'malo omwe sanabzalidwe? Imeneyo inali mbewu yoyipa ikuchulukana.

WISDOM'S HOUSE MINISTRIES 2021

How to Grow in the Lord Lesson2 Outline



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

Mulungu akabzala mbewu yake yabwino mwa ife, amayembekezera zotsatira zomwezo. Amayembekezera kuti adzakula ndi kuchulukitsidwa. Kodi tingachulukitse bwanji zipatso zathu kwa Yehova? Pa 2 Timoteo 2:2 mtumwi Paulo akuuza Timoteyo kuti aphunzitse zonse zimene waphunzila kwa amuna ena okhulupilika kuti akwanitse kuphunzitsanso ena. Mulungu akufuna kuti titenge chipatso chabwino chimene anachikuzana m'miyoyo yathu ndi kugawana ndi ena mmawu ndi m'zochita. Umo ndi momwe mbewu yabwino ya Mau a Mulungu imachulukira.

Kodi mukuchulukitsa mbewu yamtundu wanji?

Kufananitsa a Chipatso cha Mbewu ndi Makhalidwe Anu

Yesu akuti mu Mateyu. 7:15-20 “Mudzawazindikira ndi zipatso zawo. Kodi ankatanthauza chiyani pamenepa? Kodi izi zikutanthauza kuti chipatso chilichonse chili ndi dzina la munthu? Ayi. Zikutanthauza kuti mungadziwe mtundu wa zipatsao za munthu pakuona zomwe munthu amalankhula ndi kuchita. Zipatso zoipa ndi zofanana ndi makhalidwe oipa. Zipatso zabwino ndi zofanana ndi makhalidwe abwino.

Musanyengedwe, chimene munthu wafesa, chimenechonso adzachituta!!

Mwachidule

Mulungu akufuna kuti tilole ena kulawa chipatso chimene talima mwa ife kuti abzale ena mwa iwo okha mu mtima mwawo. (Kugawana, Kuchulukitsa).



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

Phunziro #6 Zochitika

Kuchulukitsa Mbewu

Ntchitoyi itithandiza kuwonetsa momwe chomera (chabwino kapena choyipa) chingaonjezekere (kuchuluka) kutengera kuchuluka kwa njere zome ili nazo.

Zomwe mungafunikire

- ☐ zipatso zingapo zosiyanasiyana zomwe zili ndi njere
- ☐ udzu wambiri wokhala ndi njere
- ☐ mpeni

Zoyenera kuchita

Dulani mitundu yosiyanasiyana ya zipatso ndikuchotsamo njere zonse. Uzani mwana wanu kuti awerenge kuchuluka kwa njere zomwe zinapangidwa ndi chipatso chimodzicho. Kutengera ndi njere zomwe zilipo, lolani mwana aliyense anene kuti ndi zipatso zingati zomwe zingapangidwe. Iyi ndi nkhani ya masamu kwa ana okulirapo. Auzeni kuti aonere kuti ndi zokolora zochuluka bwanji zoyembekezedwa za mbewu



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

iliyonse. Kodi zokolola zikanakhala zotani pakatha nyengo yokolora imodzi? nanga pa nyengo zokolora ziwiri?

Idyani zipatso mwachimwemwe limodzi ndi mwana wanu pamene mukukambirana mmene mukupindulira ndi khama lanu. Zokolola zake zinagawidwa ndi anthu ambiri (pogulitsa). Akhoza kugawana ndi ena. Chifukwa cha kukoma kwachipatsocho, ena atha kupita kukapeza zipatso zawo.

Fanizo lomweli lingawiritsiridwe ntchito pofotokoza za mbewu imene Mulungu anabzala mwa ife. Ngati tigwira ntchito molimbika kuti mbewu zathu zikule ndikubereka zipatso zabwino (onani Chipatso cha Mzimu mu Agalatiya 5:22-23) Tikamagawira ena zipatso zimenezi, tikhoza kukhudza anthu ambiri. Akhoza kulawa zipatso zathu ndipo angafune kupeza zawo.

Phunziro lomweli likufotokozanso za udzu. Chotsani njere zambiri za udzu. Werengani njerezo. Lankhulani ndi mwana wanu za kuchulukitsa mbewu zoipa. Gwiritsani ntchito nthawi kutchula za kusankha mabwenzi abwino osati kucheza ndi anthu amene amaonetsa zipatso zoipa.

Pamapeto onani, ndi ziti zomwe zinali ndi mbewu zambiri, zipatso zabwino kapena zoipa? Nanga chifukwa chiyani?



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

Phnunziro #7

NDEMANGA

MUNDA WA MPESA WOPANGIDWA NDI MUNTHU

Lemba la Yesaya 5:1-7, 12, 13 limafotokoza za munthu amene anabzala mpesa. Nkhani iyi ikufotokoza mwachidule phnunziro lathu la kakulidwe ka zomera.

Mwachidule, Zinkawoneka kuti munthuyo anachita zonse zoyenera kuti akolole mphesa zabwino, koma chinachake chinalakwika. Werengani za mundawo wa mpesawu limodzi ndi ana anu ndikusankha zinthu zosiyanasiyana za kakulidwe ka mbewu zomwe zimafunika kuti zikule bwino.

“... Wokonedwa wanga anli ndi muknda wa mpesa pa phiri la nthaka yachonde, atatipula anachotsa miyala yonse (khama kuchotsa miyala) ndipo anawokamo mipesa yabwino kwambiri (mbewu yabwino) anamanga nsanja yolondera pakati pa mundawo ndipo anasemanso mopsinyira mpesa mmunda mommwemo. Ndipo iye amayembekeza kuti mundawo mudzakhala mphesa zabwino kwambiri koma ayi unabala mphesa zosadya (zipatso zapanyengo). Tsopano inu anthu a mu Yerusalemu ndi inu anthu a ku Yuda weruzani pakati pa ine ndi munda wangawu, kodi ndidakawuchitira chani china munda wangawu kuposa izo nnachita kale? Pamene ndinkayembekezera kuti udzabala mphesa zabwino, bwanji unabala mphesa zosadya? Yesaya 5:1-4

Kodi mungayankhe funso la munthuyu? N’chifukwa chiyani anakolola mphesa zoipa? Kodi anatsatira njira zonse zomwe zimathandizira mpesa kukula bwino? Kodi akanaphonya chiyani? Vesi 5 ndi 6 limanena za kukhudzika koonekeratu kumene munthu ameneyu anali nako pamene sanalandire zokolola zimene ankayembekezera.

Kodi zipatso zabwino zimene Mulungu amayembekezera kwa anthu ake zinali zotani? (:ndimei 7) Nanga ndizipatso ziti zomwe anzipeza? (ndime: 7 ndi 8.)



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures











“Tsopano ndikuuzani chomwe ndidzauchite munda wanga wa mphesa, ndidzachotsa mpanda wake, ndipo nyama zidzapondapondamo, ndidzausandutsa tsala, udzakhala wosatengulira ndiwosalimira ndipo mudzamer nkandankhuku ndi minga zina, ndidzalamula mitabo kuti isagwetse mvula pa mundapo” Yesaya 5:5,6

M’maphunziro onse apitawa, takambirana matanthauzo a kuthupi ndi uzimu okhudza kulima mbewu. Pogwiritsa ntchito maso athu munthuyu akanatha kulima mphesa zabwino. (onani Mateyu 13:24-30 kuti mumve nkhani yofanana ndi imeneyi) Kuyang’ana pa nkhanayi kudzera m’maso athu auzimu kukupereka chithunzi chosiyana kwambiri. Mu vesi 12 ndi 13, Yesaya akuti

“...“...Saona chimene Yehova wachita, saona ntchito ya manja ake; kotero kuti anthu anga adzalandidwa, natengedwa, chifukwa sadziwa ine; akulu onse adzafa. anthu wamba adzafa ndi ludzu (mizu yosatunga madzi).”


Kulima mbewu ndi mgwirizano. Munthu ali ndi gawo lake, ndipo Mulungu ali ndi gawo lakenso. Ngati timuyiwala lye ngakhale mbewu zathu zakuthupi kapena zauzimu sizidzakula kukhala zomwe timayembekezera.

Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

masitepe	Zizindikiro	Mkhalidw e wathupi	Tanthauzo la uzimu	Chomera choyamba	Chomera chachiwiri	Comera chachitatu	Chomera chachinayi
Nthaka		Yolimba/y ofewa		Chodziper eka (chofewa)	Chodziper eka (chofewa)	Kusadziper eka (kulimba)	Chodziper eka (chofewa)
Mbeu		Yosakanizi ka/ yangwiro		Changwiro	Chodetsed wa (kusakaniz a)	Changwiro	Changwiro
Ofesa		Yosalimid wa/ yolimidwa		Kulimbika (Yolimidw a)	Changwiro	kufooka	Walesi (yosalimid wa)
Nyengo		Thaka yolimba / nthaka yofewa		Kudalira (nthaka yofewa)	Yoskhulupi lika (chifooko)	Yokufa	Kufa
Chipatso mu nyemngo yake		Zipatso zoipa/ zipatso zabwino		Chipatso chabwino	Hipatso choipa	yokufa	Yokufa



Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures





Finding shelter from the Current Social Storms in two Hidden Biblical Structures

